

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

KUITANIDWA KUTI TITUMIKIRE

Masiku ano, pali kufunikira kwakuti anthu amene angakhale otumikira mu mpingo akhale okhulupirika. Pali zinthu zofunikira zakuthupi komanso zakuuzimu zimene zilipo zomwe mpingo ukuyenera kulimbana nazo. Pali zopereka zimene zifunika kuti zitoleredwe ndi kugawidwa, pali ntchito yokonza ndi kutsuka nyumba ya Mulungu, pali zochitika zimene zifunika kuzilongosola. Komanso pali odwala ofunika kuyenderedwa ndi osauka ofunika kuti athandizidwe. Umakhala mdalitso waukulu ku mpingo wa Khristu ngati pali otumikira okhulupirika ndi opezeka nthawi zonse amene amagwira ntchito ngati izi mwachete ndi modalirika.

Moyo wokoma ndi wautali wa mpingo umayezedwa chimodzimodzi ndi kuchuluka kwa ntchito zimene otumikira okhulupirika amazigwira komanso m'mene amachitira abusawo pamodzi ndi utumiki. Mu mpingo yambiri, ntchito yolemetsa ya zinthu zooneka ndi maso komanso zauzimu imatsamira pa mapewa a utumikiwo. Pamene utumiki utanganidwa kwambiri ndi ntchito za mpingo zooneka ndi maso, maganizo komanso mphamvu zao sizikhazikika pa zinthu zauzimu. Si udindo komanso ndi si chinthu chimene chikuyenera kuyesedwa chamwai pamene akhristu a mumpingo adzipereka kuti atumikire. Khristu anatisiyira chitsanzo choposa cha kukhala wotumikira pamene anati, "Pakuti ndithu, Mwana wa Munthu sanadze kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la kwa anthu ambiri" (Marko 10:45).

Monga m'mene nyumba imayenera kusamalidwa ndi kukonzedwa kosaleka, chimodzimodzinso nyumba imene ikugwiritsidwa ntchito ngati yopemphereramo. Nthawi zambiri ntchito ya uthenga wabwino imatchingidwa chifukwa zinthu zooneka ndi maso za pa mpingopo sizili m'malo mwake. Ha! Taonani kukoma kwake pamene tiona anthu a zaka zosiyanasiyana akutenga udindo mu

thupi la Khristu ndiponso akutumikira mwa iwo okha koma pofuna kuti mpingo upindule. Nyumba yopemphereramo imene ili yosamalidwa bwino ndiponso kayendetsedwe kabwino ka ntchito za mpingo umakhala umboni wabwino ku dziko lapansi.

Pa 1 Akorinto 4:2 akunena kuti: "Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika." Mulungu wawakhulupirira anthu ake osati ndi uthenga wauzimu okha komanso ndi kutumikira ngakhalenso kufikira ku zosowa za ena. Nkosavuta kuti pafupipafupi anthu adzipereke, koma ndi chinthu china chapaderadera kuti iwo agwire ntchito mokhulupirika ndi kutumikira kwa miyezi ingapo opanda kuthokozedwa kapena kungothokozedwa mwa pang'ono. Oyera mtima a Mulungu akuitanidwa kuti agwirire ntchito Ambuye; zimene zikutanthauza kuti kukhutira ndi kukwaniritsidwa kwao kudzichokera mu kukondweretsa Mulungu osati chivomerezo cha munthu. Ntchito ya wotumikira makamaka siyosangalatsa, koma ndi yofuna kukondweretsa Iye amene timtumikira.

Kaya ndi mtumiki, kaya ndi oyang'anira kapena mphunzitsi wa Sunday school, wotsogolera nyimbo, woimba wapaderadera, wophika, lebala kapena mkhristu chabe mu mpingowo. Kutumikira modalirika ndiponso kupezeka kuti tichite chofunikiracho ndi zinthu zimene zingathandizire kuti ntchito ya uthenga wabwino iyende bwino komanso ndi zinthu zopambana kwambiri makamaka ngati tikufuna kukhala ndi mpingo wathanzi. Mulungu wawadalitsa anthu ake ndi maluso komanso nzeru zosiyanasiyana. Pakhoza kukhala zinthu zochepe chabe zimene zingafunikire mu ntchito yathupi komanso yauzimu ya mpingo kutakhala

(Yapitirira pa tsamba 2)



**"Moyo wokoma
ndi wautali
wa mpingo
umayezedwa
chimodzimodzi
ndi kuchuluka
kwa ntchito
zimene otumikira
okhulupirika
amazigwira
komanso m'mene
amachitira
abusawo pamodzi
ndi utumiki."**

Zoyenera kuchokera
M'malemba za
Atumiki

2

Mau a Mkonzi

Atumiki a Mulungu
ndi ndalama

3

Udindo wa Mtumiki

4

Funso Yanko

7

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

kuti anthu akupereka kwathunthu nthawi ndi maluso ao ku ntchito ya Mulungu. Chimwemwe komanso madalitso a Mulungu nthawi zambiri zimatsamira pa kudzikhuthula, pa kupereka ndiponso kutumikira.

Kwezani maso anu ndipo muone ntchito imene ili pakati panu ndipo mudzitenge inuyo kukhala wotumikira wa Ambuye wokhulupirika. ■

Zoyenerereza kuchokera M'malemba za ATUMIKI

(1 Timoteo 3:8-13 ndi Machitidwe 6:3)

- Odzazidwa ndi Mzimu Woyera.
- Olemekezeka.
- Osamwetsa vinyo.
- Wodzisunga ndi Wodziletsa ndi Wolongosoka.
- Osakhala ndi dyera la ndalama.
- Okhala nacho chikhulupiriro choona.
- Okhulupirika.
- Oyesedwa kuti akhoza kutumikira. Asakhale wophunza.
- Odzazidwa ndi nzeru.
- Ambiri yabwino.
- Opanda chifukwa.
- Mwamuna wa mkazi mmodzi (mitala ndi chigololo zili zoletsedwa).
- Mkazi akhale wa mbiri yabwino, wolemekezeka, wokhulupirika ndi wosanena miseche.
- Wakukhala nao ana ake omvera iye.
- Akusamala ndi kuyang'anira bwino nyumba yao.

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



“Two amene ali atumiki a zinsinsi za Yesu Khristu akuyenera kukondwera anthu onse mu njira zonse. Popeza iwowo sali atumiki a nyama kapena zakumwa [zokha] koma atumiki a mpingo wa Mulungu.” (*Kalata ya Ignatius kupita kwa Trallians*, mu zaka za ma 100-200AD).

Mutu wathu ulendo ndi wa udindo wa atumiki. Iyi ndi nkhani yofunikira kwambiri, ndipo ndikutsimikizika kuti ikanakhala kuti anthu anaimvetsetsa bwino ndi kuitenga kukhaladi yofunikira, ntchito ya uthenga wabwino ikadayenda mwa myaa ndipo mipingo yambiri mwenzi ili pabwino. M'mene ndinali pakatikati pa kafukufuku wanga pa nkhanayi ndi pamene ndinazindikira kuti mutuwu ndi wovuta ndithu. Sipanapite nthawi, ndimawerenga za Mpingo wa Atumwi ndipo ndinapeza pena pamene C. E. Brown naye anatsimikiza chimodzimodzi ndipo anati: “Kuphunzira za udindo wa mtumiki ndi chinthu chovuta chimene ndiyesa kuti ndi chovuta kwambiri kusiyana ndi gawo lililonse la mbiri ya Mpingo woyamba.”

Vutoli limabwera chifukwa pali zinthu zochepa kwambiri zimene zinanenedwa zokhudza zimene udindowu umayenera kuchita ndipo tikuyenera kuphatikiza zowerenga zochepa zimene timazipeza m'Malemba ndi zimene zili mu mbiri ya mpingo woyamba kuti timvetsetse za nkhanizi. Atumiki ndi ofunikira ku ntchito yonse imene imachitika mu mpingo wa Church of God. Ngakhale kuti aliyense amaitanidwa kuti atumikire, nchodziwikiratu kuti pali anthu amene amatumikira ngati atumiki mu mipingo koma sanapatulidwe ku udindowo. Anthu awa amene amva maitanidwe apadera a Mulungu ku utumiki ndi utsogoleri wauzimu umene umaposa nthawi imene munthu amakhala pa udindo wa woyang'anira kapena msungichuma. Awa ndi ena mwa anthu okhulupirika ochepa amene ali wokhazikika ndi wolimbikira, nagwira mwakhama ntchito yoyang'anira zofunikira zakuthupi za mpingo ndiponso kupereka thandizo la uzimu ndi lokhazikika ku ntchitoyi. Mtumiki penapaliponsepo ndi mtumiki ndithu, koma pali phindu mu kuzindikira maitanidwe a Mulungu ku udindo uwu waumulungu mu mpingo monga mwa chitsanzo chimene timachipeza mu Malemba. Pasakhale chisokonezo, mpingo wa Mulungu ulibe utumiki wochita kukhala ndi dzina, komanso sukhalani ndi atumiki odziwika ndi dzina. Maudindo awa kwambiri amakamba za kutumikira Mulungu, osati chifukwa m'mene amaonekera, kudziwika ngakhale udindo umene ali nao. Chofunikira kwambiri kusiyana ndi udindowu ndi mtima wachikondi wodzichepetsa ndi wotumikira.

Ngakhale kuti mutuwu waipitsidwa ndi chiphunzitso chonama komanso ndondomeko ya kayendetsedwe ka mpingo monga amachitira a Chikatolika, udindo wa mtumiki wakhala uli gawo la mpingo wa Mulungu kuyambira nthawi imene atumwi anayamba kutsogolera mpingo. Ndikofunikira kuti chiphunzitsochi ndiponso machitidwe oterewa apitirire. Pali kumvetsetsa molakwika pa zimene anthu amaganiza za atumiki. Anthu ambiri amaganiza kuti mtumiki ndi munthu amene ali wokalamba ndipo wakhala mu mpingomo kwa nthawi yaitali ndipo ali ndi ulamuliro, mwakuti mbusa atati wachoka ndipo sakutumikiranso, atumikiwo amakhalabe pompo. Komabe, mtumiki ndi munthu amene amatumikira mokhulupirika pothandizira utumikiwo polimbikitsa gawo la kuthupi ndi la kuuzimu la mpingowo. Atumiki akuyenera kugonjera ndi kumvera ulamuliro wa utumiki ndiponso kuti anthu amulemekeze amene amatumikira Mulungu modzichepetsa. Mtumiki wabwino ndi wokhazikika ndi wochita zinthu mwanzeru, napereka kwa onse chitsanzo chabwino cha kutumikira.

Mulungu adalitse mpingo wa Church of God ndi kumvetsetsa kwakukulu kwa zochitika za udindo wokhala mtumiki.

Michael W. Smith

October 2020

Atumiki a Mulungu ndi NDALAMA

Atumwi anauza mpingo wa ku Yerusalemu kuti usankhe amuna 7 kuti adziyang'anira ntchito zachuma za mumpingo. Izi zinadza chifukwa Agriki amadandaula kuti panali kukondera pa kagawidwe ka zachifundo. Ngakhale kuti sizingachitike nthawi zonse, komabe chimakhala chanzeru kuti mtumiki wa Mulungu afutuke pa kukhala woyang'anira kapena kumagwira nawo ntchito zokhudza chuma cha mpingo wake poopa kuti mdaniyo akhoza

kulowererapo. Zikatero mtumiki wa Mulunguyo amakhala womasuka kuti akhoza kulalikira posalabadira kuti kodi ndi ndani amene akumuthandiza kugawo la zachuma. Motsatira ndondomeko imene ili m'malemba, mtumiki wa Mulungu, monga m'mene angakwaniritsire, adzilola kuti amuna a mbiri yabwino mumpingo apatsidwe ntchito yoyang'anira chuma cha mpingo wake.

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

UDINDO WA MTUMIKI

Ngakhale kuti pali mphatso zauzimu zambiri, maudindo a mkuluwampingo ndiponso mtumiki ndi maudindo awiri amene amapezeka molingana ndi Baibulo mu mpingo wa m'Chipangano Chatsopano mu onena za utsogoleri ndi ntchito motsogozedwa ndi ulamuliro wa Mzimu Woyera (1 Timoteo 3:1, 8).



Mu Malemba, udindo wa woyang'anira ndi wofanana ndi wa mkuluwampingo ndipo ndi mau amene amagwiritsidwa ntchito pofuna kunena za iwo amene anaitanidwa ndi kuyenerezedwa kuti akhoza kumalalikira Mau a Mulungu. Pali zitsimikizo zambiri zosonyeza kuti oyang'anira ndi akuluwampingo anali amodzi, ndipo zinali chomwecho kufikira pamene chiphunzitso chonyenga cha Chikatolika chinabweretsa kusiyana pakati pa maudindo awiriwa.

Udindo wachiwiri ndi wa mtumiki. Atumiki anali iwo amene amatumikira ku ntchito yathupi ya mpingo ndipo amathandizira akuluwampingo. Zomuyenereza mtumiki zinali zofananirako ndi izo za woyang'anira komanso panali chimodzi chokha chosiyana chakuti oyang'anira akhale “wokhoza kuphunzitsa.” Ndi udindo wosankhidwa kuchokera kumwamba ndipo umene anthu ake akhale kuti ndi odzazidwa ndi Mzimu komanso okhala ndi zowayenereza.

Zimene Mabuku ena anena

Pamene tikusanthula Baibulo pa nkhani yokhudza udindo wa utumiki zikhoza kukhala zovuta komanso popeza Baibulo limaphunzitsa mwachimvekere za udindo ndi zoyenereza zake. Komabe silifotokoza motambasula bwino zonse zokhudza ntchito ndi kayendetsedwe ka udindowo. Mulungu amasamalira kwambiri za khalidwe la mtumikiyo kusiyana ndi zoyenerera za ntchitoyo. Nkofunikira kwambiri kuti maudindo awiri awa tiwamvetsetse mosawasiyanitsa poopa kuti tikhoza kuwaika mwabwinobwino mwakuti pasapezeke wina ooneka wamkulu ndi wofunikira kuposa unzake pa kayendetsedwe ka mpingo monga zimachitira mu mpingo wa atumwi. Chifukwa cha ichi, nkofunika kusanthula bwino zimene zinalembedwa mu Baibulo ndipo tiziunguze molingana ndi mbiri komanso poganzira gawo lauzimu ndi zosowa zakuthupi za mpingo.

Tanthauzo

Mau akuti Mtumiki amachokera ku chinenero cha Chigriki otchedwa *diakonos* ndipo amatanthauza wothandiza, wotumikira pamene anthu akudya, wotumikira, wantchito (*Strong's Dictionary/Thayer's Greek Definitions*). Mau akuti *diakonos* amagwiritsidwa kokwana ka 30 mu Chipangano Chatsopano ndipo amatanthauziridwa mosiyanasiyana molingana ndi ndimeyo. Ndi malo ochepa amene mauwa amagwiritsidwa ntchito kunena za udindo wodziwika wa Mtumiki. Talingalirani malemba owerengeka pofuna kulongosola chabe. Pa Mateyu 20:26 akuti, “koma aliynse amene akafuna kukhala wamkulu mwa inu, adzakhala mtumiki [*diakonos*] wanu.” Pa Aroma 13:4 akunena za olamulira aboma ngati atumiki [*diakonos*]. Paulo analankhula za kukhala m'moyo “umene anandikhalitsa mtumiki wake monga mwa mphatso ya chisomo cha Mulungu” (Aefeso 3:7). *Diakonos* amatanthauziridwa “mtumiki” mu ndime zingapo. “Koma wamkulu wopambana wa inu adzakhala mtumiki wanu [*diakonos/deacon*]” (Mateyu 23:11). Antchito a mfumu, amene amatumikira pa matebulo mfumu ikudya, amatchedwanso kuti *diakonos* pa Mateyu 22:13 ndi pa Yohane 2:9. Zikuchita kuonekeratu kuti *diakonos* amagwiritsidwa ntchito pofuna kuonetsa kuti pali ntchito ndi mautumiki osiyanasiyana, ndipo mu malo osiyanasiyana oyera mtima amatchedwa atumiki a Mulungu.

Udindo wa Mtumiki

Mau akuti *Diakonos* anayamba kuoneka phindu lake pamene Paulo anawalembera akhristu a mpingo wa Afilipi mchaka cha 62 AD. “Kwa oyera mtima onse mwa Khristu Yesu, akukhala ku Filipi, pamodzi ndi oyang'anira ndi atumiki” (Afiipi 1:1). Paulo akuwalembera oyera mtima ndipo akutchulapo maudindo awiri mu mpingo, amene ali oyang'anira (akuluwampingo) ndi atumiki. Malonje amenewa ndi ofunikira pofuna kumvetsetsa dongosolo ndi adindo a mu mpingo woyamba. Ntchito ya atumiki ikudaliridwa ndi

Mtumiki
amatanthauza
wothandiza,
wotumikira pamene
anthu akudya,
wotumikira,
wantchito.

kuvomerezedwa pamene pa 1 Timoteo 3 Paulo akupereka momveka bwino za zomuyenereza munthu pa udindo wa mtumiki. “Ngati munthu akhumba udindo wa woyang'anira, aifuna ntchito yabwino. Ndipo kuyenera woyang'anira akhale wopanda chilema...Momwemonso atumiki akhale...” Pa nthawi imene Paulo amalemba makalata ake, nchodziwikiratu kuti panali udindo wokhazikika ndi wovomerezeka wa utumiki umene tanthauzo lake limaposera kungotumikira chabe kuthupi.

Kufunikira kwa Udindowo

Tsopano popeza tayala maziko akuti atumiki analipo mu nthawi imene atumwi anali kugwira ntchito, funso ndi lakuti, “Kodi cholinga cha mtumiki ndi chiyani?” Ngakhale kuti Malemba sanena mwachindunji zinthu zonse, zina timapeza kuchokera ku zitsanzo zimene zili m'malemba. Maitanidwe aakulu a Khristu anali akuti iye akalalikire uthenga wabwino. Komanso Iye anaphunzitsa ophunzira ake kuti adzithandiza osauka ndi kutumikira ku zosowa za iwo amene alibe. Yesu ndi ophunzira ake anali kuthandizidwa ndi chuma chimene anthu ena amapereka (Luka 8:3). Panali kufunikira kwakuti winawake adziyang'anira chumacho ndiponso zopereka. Zikuoneka kuti Yudasi ndi amene amanyamula thumba m'mene munali ndalamazo (Yohane 12:4-6) ndipo anali ndi udindo wogula zonse zofunikira pa utumiki komanso kuthandiza osauka (Yohane 13:29). Izi zikutionetsa kuti pali kufunikira kwakuti wina wake akuyenera kumayang'anira ntchito yosamalira chuma.

Kusankhidwa kuti atumikire

Litadutsa tsiku a Pentekoste, mpingo unakula mwachangu, ndipo atumwi samangolalikira za uthenga wabwino okha komanso amatangwanika ndi kayendetsedwa ka zachuma mu mpingo. Zimene zalembedwa mwatsatanetsatane pa Machitidwe 6:1-6 ndi zomwe zinachititsa kuti pakhale udindo wa mtumiki.

Koma masiku ao, pakuchulukitsa ophunzira, kunauka chidandaulo, Agriki kudandaula pa Ahebri, popeza amasiye ao anaiwalika pa chitumikiro cha tsiku ndi tsiku [diakonia/ utumiki]. Ndipo khumi ndi awiriwo anaitana unyinjwa wa ophunzira, nati, Sikuyenera kuti ife tisiye kulalikira mau a Mulungu ndi kutumikira [diakoneo/mtumiki] podyerapo. Chifukwa chake, abale, yang'anani mwa inu amuna asanu ndi awiri a mbiri yabwino, odzala ndi Mzimu ndi nzeru, amene tikawaike asunge ntchito iyi. Koma ife tidzalimbika m'kupemphera, ndi kutumikira mau. Ndipo mau amene anakonda unyinjwa wonse; ndipo anasankha Stefano, ndiye munthu wodzala ndi chikhulupiro ndi Mzimu Woyera, ndi Filipo, ndi Prokoro, ndi Nikanore ndi Timoni, ndi Parmenasi, ndi Nikolasi,

ndiye wopinduka wa ku Antiokeya: amenewo anawaika pamaso pa atumwi; ndipo m'mene adapemphera, anaika manja pa iwo.

Amuna 7 awa anaikidwa kuti azitumikira podyerapo, kapena kunena kuti akhale adindo a ndalama ndiponso zinthu zina zakuthupi zimene zimafunikira ku mpingo wa ku Yerusalemu.

Ngakhale kuti zolemba zoyambirira zikuwatchula iwo ngati atumiki oyamba (zomwe analemba Irenaeus mu zaka za ma 100AD), naye Luka mu buku la Machitidwe sakuwatchula amuna 7 aja kuti atumiki. Chifukwa cha ichi, pakhalabe pali kusutsana pa nkhani imeneyi. Komabe nkofunika kudziwa kuti panthawiyi mpingo unali ukukula. Zimene tikuziona mu Machitidwe 6 zikungoonetsa pang'ono za udindo ndi kufunikira kwa ntchito ya mtumiki, imene itakhwima ndi kuzika mizu inadzanenedwa motambasula bwino pa nthawi Paulo amalemba kalata yake ya 1 Timoteo.

Ntchito ndi Maudindo

Mwachidule, atumiki ali oitanidwa ku uzimu ndipo amayenerezedwa kuti atumikire mu mpingo. Katswiri uja wa mbiri yakale komanso zaumulungu Adam Clarke analemba motere zokhudza atumiki: “Udindo wa mtumiki, mu mpingo wakale, unali wa kutumikira mu *agapae*, kapena zikondwerero zachikondi, kugawa mkate ndi vinyo kwa okhulupirira, kulengeza za nthawi ndi magawo a chipembedzo m'mpingo ndiponso kusamalira amai amasiye, ana amasiye, andende ndi odwala amene amathandizidwa kuchokera mu thumba la mpingo....Iwo anali kusamalira osauka, ndi kulalikira pafupipafupi” (*Adam Clarke Commentary*, Mateyu 20:26).

Adindo wa zinthu zathupi

Imodzi mwa ntchito zazikulu za mtumiki ndiko kukhala woyang'anira chuma cha mpingo ndipo palibe amene amatsutsa za ichi. “Mu masunagoge akale a Ayuda panali anthu atatu amene anapatsidwa ntchito yoyang'anira osauka....kuchokera kwa adindo amenewa mwina atumwi anatengako ganizo losankha atumiki a mpingo wa Chikhristu, ndipo ndi zosakaikitsa kuti iwo amafuna kuti ntchito zao zikhale zofanana” (*Albert Barnes' Notes on the Bible*, Machitidwe 6).

Poyambirira, amuna 7 aja anapatsidwa udindo woyang'anira ntchito yogawa zakudya kwa osauka ndi kuyang'anira chuma cha mpingo.

(Yapitirira pa tsamba 6)



“Atumiki ali oitanidwa ku uzimu ndipo amayenerezedwa kuti atumikire mu mpingo.”

(Kuchokera pa tsamba 5)

Maudindo ao ena anayamba kuchuluka pamene nthawi imapita ndipo ntchito ya utumiki inasintha mu mbiri ya mpingo kuyambira kwa Akatolika komanso ma Protestant, ndipo izi zinachitika makamaka mnjira za mpatulo ndi zathupi. M'bale Ed Wilson, mkulu wa mpingo wa Church of God, analemba kuti: “Sikuti nkoyenera kuonetsa kusiyana kwenikweni kwa maudindo ndi zochitika zimene zili zololedwa, ntchito zautumiki zauzimu ndi zathupi zimalowerana mosavuta ndiponso mopanda mikangano chifukwa zochitika zonse zimachokera ku mitima yoyera imene cholinga chake chachikulu ndicho kutumikira mulimonse ndi kwa wina aliyense.” Tikuyenera kusamalitsa pamene tikufunzulula maudindo ena, komabe pali zimene timadziwa ndiponso zochitika za udindowo zimene sizilembedwa mu Baibulo, koma zili zogwirizana ndi chifuniro cha Malemba.

Udindo wa Mtumiki ndi wolingana ndi matumikiridwe, ndipo pali ntchito zina zakuthupi zimene zili zochitika sabata iliyonse ndipo zimafunikira kuziyang'anira mumpingo (monga kusamalira zinthu za pa mpingo, kugwira ntchito zosiyanasiyana zamanja, kuthandizira zida zokweza mau ndi zina zotere). Maudindo awa akhoza ndipo amasaliridwa ndi mamembala amene sali opatulidwa, komabe iwo amakhala pansu pa ulamuliro wa mtumiki. Ndi udindo wa utumiki kuyang'anira chuma ndiponso zopereka zachifundo za mpingo. Atumiki akuyenera kunena ku mpingo zimene zikufunikira ndipo aonetsetse kuti zopereka zatengedwa pafupipafupi kuti zithandizire zosowekera zina ndi zina, zothandizira osowa komanso utumiki. Ndalama zonse zikuyenera kugawidwa mwachilungamo ndi mosakondera. Nthawi zambiri abusa ndi mpingo avutika chifukwa utumiki sanakhulupirike pa maudindo ao.

Othandizira ku utumiki


Nkofunikira kudziwa kuti amuna 7 aja amene akutchulidwa pa Machitidwe 6 anasankhidwa ndi mpingo, natsimikizidwa ndi atumwi, ndipo anasankhidwa ndi cholinga chakuti athandizire ndi kupeputsa atumwi pa zina mwa ntchito zao. Potengera izi ngati chitsanzo kapena poyambira, nzochita kuonekeratu kuti nkupita kwa nthawi, maudindo a mtumiki anapyola pongotumikira zakuthupi basi. Mtumiki weniweni ndi iye amene sangotumikira ku magawo a thupi, koma ndi thunthu lofunikira la utumiki, ndi kuthandizira pena paliponse pamene pangafunikire.

Utsogoleri wokhulupirika ndi wauzimu

Chifukwa chakuti pamafunikira kukhala ndi zoyenera zauzimu zosafikirika wamba komanso kuti anthu amudalire munthuyo, utumiki amapereka utsogoleri wakuthupi ngakhale wakuuzimu mu mpingomo. Pakakhala kuti mbusa palibe, mtumiki ndi amene anthu amamudalira. Atumiki ndi anthu amene ali ndi zowayenera kuuzimu kuti akhoza kutsogolera zipembedzo ndiponso kuthandiza poonetsetsa kuti akusungitsa bata mumpingo ngati pali pofunika kutero. Iwo amathandizira kukonza ndi kuyendetsa misonkhano ndipo amakhala ngati ulalo pakati pa akuluampingo ndi mpingowo. Adam Clarke ananena chinthu china chokhudza utumiki chimene chili chosangalatsa kwambiri kuti iwowo “amalalikira pafupipafupi.” Atumiki ena akhoza kukhala alaliki a Mau monga amachitira Stefano ndi Filipo mu buku la Machitidwe. Atumiki okhulupirika amaima pampata maka pamene mpingowo ulibe mbusa ndipo mosaonetsera amasenza udindo oonetsetsa kuti akuluampingo akuphunzitsa m'choonadi ndi m'chiyero.

Udindo wa mtumiki unasanduka wachikunja komanso wandale chifukwa cha kukula kwa mpingo wa Chikatolika. Tikuyenera kudziwa kuti mpingo wa Chikatolika poyamba penipeni umakaniza utumiki kuti asapereke ukaristiya koma umawaloleza kubatiza ngati mkuluwampingo palibe kapenanso ngati “palibe kuchitira mwina.” Kumvetsetsa komanso maganizo anga pa nkhanayi monga wolemba ndiko kwakuti pakati pa oyeramtima a Mulungu, utumiki akhala ndipo akhoza kuthandiza pa ubatizo kapena kudiyetsa mgonero wa Ambuye ngati mkuluwampingo wamupempha kutero. Ndi udindo waukulu wa utumiki a Mulungu kuti adzichita ntchito zimenezi, komabe pamene pafunikira iwo akhoza kuthandizidwa ndi utumiki (amene ali ngati wotumikira chabe).

Oyera mtima onse akuitanidwa kuti apereke chuma chawo komanso iwo eni adzipereke ku uthenga wabwino mu moyo wotumikira. Komabe mtumiki ali ndi maitanidwe komanso malo apaderadera akuti awafikire mu thupi la Khristu. Iyi sinkhani yokhudza maudindo amene anthu amapatsana kapena maulemu koma kufunafuna kukondweretsa Mulungu kudzera mu moyo wodzipereka kwa anthu ake. Mtumiki wokhulupirika ndi wodalirika ndi wofunikira kwambiri ngati mthandizi ku utumiki ndiponso ngati wotumikira wa mpingo wa Church of God. ■



“Mtumiki weniweni ndi iye amene sangotumikira ku magawo athupi, koma ndi thunthu lofunikira la utumiki, ndi kuthandizira pena paliponse pamene pangafunikire.”



Kodi pali kusiyana kotani pakati pa woyang'anira ndi mtumiki?

Ngakhale kuti udindo wa oyang'anira si udindo umene umanenedwa mu Baibulo, komabe udindo wa oyang'anira ndi wovomerezeka molingana ndi Malemba popeza oyanganirawo amakhala adindo. M'maiko ambiri kawirikawiri amakhala ndi lamulo lakuti gulu la oyang'anira amene akuyendetsa mpingo lidzilembetsa kuboma. Nthawi zambiri oyang'anira amasankhidwa ndi mpingo kuti atumikire kwa zaka zingapo malingana ndi m'mene malamulo a mpingowo. Oyang'anirawo amaimira mpingo kumbali yokhudza malamulo ndipo mwalamulo amakhala ndi udindo wosamalira katundu yense wamkulu wa mpingowo monga nyumba kapena magalimoto. Kawirikawiri amayang'ananso za m'mene katundu mkulumkulu kapena zachuma za mpingowo zikuyendera. Oyang'anirawo amalolezedwa kugula ndi kugulitsa zinthu m'dzina la mpingowo komanso kusayinira mapepala a umwini a mpingowo. Oyang'anirawo amakhala kuti mpingowo wawakhulupirira ndi udindo waukulu kwambiri ndipo amayenera kukhala anthu amene ali odalirika ndi oona mtima.

Nthawi zambiri woyang'anira amagwira ntchito ya mtumiki, ndipo maudindo ndi ntchito zao zimalowerana. Udindo wa utumiki ndi ntchito imene ili yovomerezeka ndi malemba, ndipo kugawo la uzimu ili ndi phindu lalikulu pa kayendetsedwe ka mpingo. Atumiki amayenera kuti akwaniritse zowayenera zimene zili pa 1 Timoteo 3 zokhudza mdindo wauzimu, pamene woyang'anira amayenera akwaniritse zoyenera molingana ndi malamulo amene mpingowo unakhazikitsa. M'bale Ed Wilson ananena kuti, "Baibulo limapereka zoyenera za atumiki, ndipo malamulo oyendetsera mpingo amapereka zoyenera za oyang'anira." Malamulo ena oyendetsera mpingo amati woyang'anira akhale ndi zoyenera za mtumiki, koma osati nthawi zonse. Maboma ena amanena kuti mipingo imayenera kuti ikhale ndi oyang'anira kuchokera ku deralo monga akatswiri a malamulo, aphunzitsi ndi ena. Zikaterere, pamafunika kuti pakhale kusiyantsa koonekeratu pakati pa malamulo amene boma limafuna ndi kayendetsedwe kauzimu ka mpingo. Monga wolemba wina analemba, "Mtumiki amatumikira ku zosowa za anthu, pamene woyang'anira amatanganidwa ndi zosowa zokhudza katundu wa mpingo."

Kodi atumiki akuyenera kupatulidwa?

Kupatulidwa kwa akuluampingo ndi mwambo komanso chiphunzitso cha mu Mpingo wa mu Chipangano Chatsopano (onani *Uthenga Wabwino*, Kalata ya No. 33). Ngakhale kuti palibe lamulo kuchokera m'malemba, komabe pali maziko a mwambo wa kupatula akuluampingo. Mu Machitidwe 6, amuna okwana 7 aja atasankhidwa, atumwi anawapemphera naika manja ao pa amunawo. Pali maganizo osiyanasiyana kuchokera kwa akatswiri a Baibulo ngati kupatulidwaku unali mwambo weniweni kapena kungotsimikira za ntchito imene iwo amayenera kukagwira. M'bale Ostis Wilson analemba motere pa nkhanayi: "Amuna 7 awa amene anali odzazidwa ndi Mzimu anasankhidwa ndi Mpingo ndipo anapatulidwa ndi atumwi ku ntchito iyi yokhala atumiki. Iwo anagwiritsa ntchito nthawiyo ndipo izi anachitika mothandizidwa ndi mphamvu komanso nzeru za Mzimu Woyera pofuna kuonetsetsa kuti zinthu zikuyenda m'njira yoyenera."

Mfundo yakuti udindo wa Mtumiki ndi umodzi mwa maudindo awiri odziwika bwino mu mpingo, kuphatikizapo kuti pali mbiri yaitali yakuti anthu akhala akupatulidwa ku udindo umenewu, zimenezi zimaonetsa kuti kupatulidwa kwa atumiki unali mwambo wovomerezeka. Kupatulidwa kumatsimikiza ndi kukhazikitsa ku mpingo maitanidwe a Mulungu kwa anthu ao amene akutumikira mu magawo akuthupi kukhala otumikira omwe ali ovomerezeka ndi odziwika ku mpingo. Sikuti ndi udindowo, koma "chimene chimafunikira ndi chakuti oyera mtima anamvetsetsa kuti iwo ngati anthu ali ndi mavuto akhoza kuwabweretsa kwa iwowo" (Ed Wilson, 2020).

H. M. Riggle (amene ali mtumiki wa Mulungu woyamba wa mu mpingo wa mu Church of God) analemba kuti: "Mu mpingo uliwonse...Ambuye amaitana anthu ena ndipo mwa Mzimu wake amawayenera iwo kuti akhale akuluampingo kapena oyang'anira. Ena amawaitana ku ntchito ya utumiki. 'Iye amaika ziwalo zonse m'thupi monga momwe Iye afunira.' Utumiki umazindikira maitanidwe awa ndipo kudzera mu kusanjikidwa manja, monga momwe amachitira atumwi ndi atumiki a Mulungu kalekale lija, amawapereka ku ntchito zosiyanasiyana iwo amene Ambuye wawasankha ndi kuwayenera. Kumeneku ndiye kumatchedwa kupatulidwa. Atumiki amasankhidwa ndi kupatulidwa kuti ayang'anire ntchito za kuthupi za mpingo" (*The Christian Church*, 1912).



KODI MUKUDZIWA?

M'busa wa ku Hermas (mzaka zapafupifupi 150 A.D.) analemba izi zokhudza atumiki: "Two amene ali ndi malo ndi atumiki omwe amagwiritsa ntchito udindo wao molakwika amaononga zimene zikanawathandizira amai amasiye ndi ana amasiye nadzilemeretsa okha kuchokera ku zolandira zomwe amapatsidwa potumikira" (Sim., IX, 26).



Mau a Nyengo Yake

MUNTHU WOSAUKA KOMA WANZERU

Yesu anaitana ophunzira ake ku utumiki wa kutumikira modzichepetsa. Mu dziko la chipembedzo limene anthu nthawi zambiri amafuna maudindo, kudziwika ndiponso kulamulira, taganizirani za nkhani iyi yokhudza munthu wosauka koma ali wanzeru imene inakambidwa ndi mfumu yakale ya ku Yerusalemu:

"Panali mzinda waung'ono muli anthu owerengeka; ndipo inadzako mfumu yaikulu, nawuzinga ndi nkondo, nkumanga malinga aakulu; koma anapezedwamo mwamuna wanzeru wosauka, yemweyo napulumutsa mzindawo ndi nzeru yake; koma panalibe anthu anakumbukira wosauka ameneyo. Pamenepo ndinati, Nzeru ipambana mphamvu; koma anyoza nzeru ya wosauka, osamvera mau ake. Mau a anzeru achete amveka koposa kufuula kwa wolamulira mwa zitsiru." Mlaliki 9:14-17.



Ha! Pakati pathu pakadakhala "anthu osauka koma ali anzeru." Zipambano pa nkondo zathu ndiponso mayankho ku mavuto athu sizibwera chifukwa chakuti anthu ena afuula kwambiri kapena ndi munthu amene dzina lake lili lodziwika. Nthawi zambiri nzeru imapezeka mwa anthu amene ali achete koma okhulupirika. Ngakhale kuti amanyozedwa ndi kupeputsidwa, komabe mau a munthu uja wosauka koma ali wanzeru anapulumutsa mzinda wonse. Ngakhale zinali choncho, iye sanakumbukiridwe kapena kupatsidwa ulemu uliwonse, ndipo anthu sanachite chikondwerero chilichonse kapena kumusangalalira, ndipo panalibe chikwangwani chimene chinalembedwa cha iye kapenanso chithunzi chake kuti aliyense adzichiona namamukumbukira ngati munthu amene anapulumutsa mzindawo. Anthu amunzindawo, ngakhale kuti anatsala pang'ono kuonongedwa, komabe anapitirira kumachita ntchito zao za tsiku ndi tsiku, ndipo munthu wosauka koma ali wanzeru uja sanamukumbukire konse.

Nthawi zambiri, ntchito ya Mulungu imapita patsogolo mwa chipambano chifukwa cha amuna kapena akazi osauka koma ali anzeru. Ntchito zao sizerengedwa kapena kutamidwa. Sakumbukiridwa kapena kuwerengedwa cifukwa cha utumiki, nzeru ndi kukhulupirika kwao; komabe kupanda iwowo, mzindawo ukanatayika. Munthu wosauka koma ali wanzeru uja sanali wotchuka kapena wodziwika, komabe mu umphawi wake iye adzipereka kuti nzeru yake ithandizire panthawi yoyenera. Mwana wa Mulungu aliyense alimbikitsidwe kuti asafunefune kutchuka kapena mphamvu koma mu umphawi wake, afunefune kukondweretsa Mbuye wake, ndipo mwachete ndi mzimu wanzeru komanso wamphamvu, atumikire anthu.

Kwa amuna ndi akazi amene ali osauka koma anzeru ndipo ali pakati pathu, tikuyamikani chifukwa cha chikondi, chisomo, nzeru ndi kutumikira kwanu, timakukondani ndi kukunyadirani. Ambuye akudalitseni! ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE